KODI PALI UTUMIKI USANU, NGATI ULIPO, ULIKUTI

NDIPO NDIPO



YOHANNE 2:22

Mtengo Wa Moyo



BEN HOWARD

©2006 Ufulu wonse ndi wotetezedwa. Bukhu iri silingagulitsidwe, kapena mwa njira iriyonse kugwiritsidwa ntchito ngati njira yopezera ndalama. Silingachulukitsidwe, kapena kutanthauziridwa mu zilankhulo zina popanda chilolezo cholembedwa kuchokera kwa:

Ben Howard
Sound Of Liberty
7286 Hwy 53W
Dawsonville, Georgia 30534 (USA)

Website Address: www.SoundofLiberty.org
Email Address: TwoAnds@SoundofLiberty.org

Lomasuliridwa Mu Chilankhulo Cha Chichewa
Ndi
Enoch Kamanula
New Testament Assembly
P.O. Box 64
Mwanza, Malawi

"Kodi Pali Utumiki Usanu, Ngati Ulipo, Ulikuti?"
Uthenga wolalikidwa pa September 7, 2008
Dawsonville, Georgia - USA

KODI PALI UTUMIKI USANU, NGATI ULIPO, ULIKUTI?

September 7, 2008

Ife tikutenga lingaliro m'mawa uno, **"Kodi Pali Utumiki Usanu, Ngati Ulipo, Ulikuti?** Potchula uthenga uwu mwa njira iyi, ife tibweretsamo zinthu zambiri zokhudza Utumiki zimene sitinazibweretsemo mwa njira imeneyi mbuyomo kuonetsera m'mene zimagwirira ntchito. Nthawi zambiri ife timamva funso lakuti kodi Utumiki Usanu uli kuti? Chabwino, m'mawa uno ife tikhala tikuona funso limenelo ndi kuliyankha ilo. Kotero ine ndikufuna ndipereke mutu woti, "Kodi Pali Utumiki Usanu, Ngati Ulipo, Ulikuti? Ndipo tikafika kumapeto inu mudzazimvetsa bwinobwino.

Ine ndikuwerenga ku Aefeso, Chaputala 4, vesi 7-16; *"Ndipo kwa yense wa ife chapatsidwa chisomo, monga mwa muyeso wa mphatso ya Khristu."* Tsopano ine ndikufuna inu muone…, pali chisomo chopatsidwa monga mwa muyeso wa mphatso ya Khristu, kotero pali muyeso pa mphatso za Khristu. Palibe muyeso wofanana pa aliyense, koma zimaperekedwa monga mwa kukhoza kwanu ndi chimene Mulungu wakuitanirani inu kuti muchite. Paulo anati, "Chisomo ichi chapatsidwa kwa ine." Iye anatinso, "Zinthu izi chitani kuti mukhale gawo la chisomo changa." Chinthu chimodzi chimene Paulo anatiphunzitsa ife kupyolera mu Utumiki wake chinali – kuti tikhale ndi lingaliro limodzi, kukhala ndi cholinga chimodzi kuti tikathe kulankhula zinthu zofanana, ndi kuti pasakhale kusiyana pakati pathu. Tsopano ngati iye anatiuza ife kuchita izo, ndiye Mulungu anapanga njira kwa ife kuchita izo. Paulo anati, "*Ndipo kwa yense wa ife chapatsidwa chisomo, monga mwa muyeso wa mphatso ya Khristu."* Ndiye apa akukamba za chimene timachitchula nthawi zambiri kuti Utumiki Usanu. Aefeso, Chaputala 4:11 akukamba za mphatso zisanu kapena ma udindo amene anaonekera koyamba mwa Khristu, kenako kupyolera mwa Paulo, kenako kupyolera mwa ena otchedwa amuna okhulupirika. Paulo akuti, "*Chifukwa chake anena, Mmene anakwera kumwamba. Anamanga ndende undende* ***napereka mphatso kwa anthu."*** Ndi pamene Khristu anabwerera ku ulemelero; Iye anasiya mphatso izi zimene zinali mwa Iye. Taonani kuti mphatso zimenezi zinali mwa Iye, koma pamene Iye anapita ku ulemelero Iye anazisiya pano. Ndipo pamene Paulo anaitanidwa ndi Mulungu, Khristu anatsanulira mphatso zimenezo mwa iye kumupatsa iye mphamvu ya kukhala Kuwala kwa Amitundu.

Tsopano Mau oti "Utumiki Usanu" ndi mphatso zisanu za Utumiki zimene Iye amapereka pano. Baibulo likuti, "Kufikitsa Oyeramtima ku ungwiro." Ine ndiwerenga monga Paulo anazilembera apa, pa vesi 11, "*Ndipo Iye anapatsa ena akhale atumwi,* (amenewo ndi oyamba) *ndi ena aneneri, ndi ena alaliki, ndi ena abusa,*

ndi ena aphunzitsi." Izi ndi mphatso zopereka mphamvu kwa wina kulalikira uthenga wabwino. Utumiki uli ngati dzanja la Ambuye. Mtumwi ali ngati chala choyamba. Tsopano chala choyamba chikhoza kukhudza zala zina zonse. Koma zala zina zonse zisingathe kukhudzana monga choncho, koma chala choyamba chikhoza kukhudza kumapeto kwa chala chirichonse, ndipo izo tikuzifanizira ndi udindo wa utumwi. Kumbukirani kuti mtumwi Paulo anali m'malo mwa Khristu ndipo iye anapatsidwa mphamvu kuti agwire ntchito mu maudindo onse awa; koma palibe aliyense wa (maudindo ena) amene angagwire udindo wa utumwi, koma zina zonse za mphatso zikhoza ndipo nthawi zambiri kugwira kupyolera mwa mtumwi; chifukwa ndi udindo umene Khristu anapereka kubweretsa Mau choyamba. Kotero choyamba atumwi, kachiwiri aneneri ndipo kenako akuti; alaliki ndi abusa ndi aphunzitsi, ndikumangozibweretsabe mu mzere.

Tsopano ife tikuona Utumiki kuonekera mwa Khristu. Koma choyamba ine ndikufuna ndiwerenge lemba lina limene ndilokhudza chimene Utumiki uli ku bukhu la Ahebri, Chaputala 3:1; patsogolo pake mu uthengawu ndikukuonetserani inu Mtumwi wamkulu ku Chipangano Chatsopano. "*Utumiki uwu* (wa Aefeso 4:11 ndi woti uchite) *wapatsidwa ku ungwiro wa Oyeramtima, ku ntchito ya Utumiki, ku Thupi la Khristu: Mpakana tonse tifike ku umodzi wa chikhulupiriro,"* ndipo ife tikuyenera kubwera ku umodzi wa chikhulupiriro…, zikutanthauza kuti tonse kukhulupirira chinthu chimodzi. Apa tikukamba za Mkwatibwi, pamene tikufika ku nthawi yotsiriza. Akuti, "*Mpaka tonse tifike ku umodzi wa chikhulupiriro, ndi chidziwitso cha Mwana wa Mulungu, ku munthu wangwiro,* (Ine ndikufuna inu muone zimenezo) *ku muyeso wa thunthu chidzalo cha Khristu:*" mwa kulankhula kwina izi zimatibweretsa ife ku kumene tikhoza kufika, mpakana tikasandulika M'modzi ndi Khristu, kumeneko ndiye kuwatiwa ndi Iye, kusandulika Mkazi Wake. Chinthu china ndichakuti tidzasinthika mu kamphindi mu kutwanima kwa diso pamene akufa adzauka, ndipo tidzakwatulidwa kukakumana naye Ambuye mulengalenga. Utumiki umenewo ndi umene tiri nawo pano mu vesi 14; akuti, "*Kuti tisakhalenso makanda, ogwedezeka gwedezeka, natengeka tengeka ndi mphepo yonse ya chiphunzitso, ndi tsenga lonse la anthu, ndi kuchenjera kukatsata chinyengo cha kusocheretsa…;*" mwakulankhula kwina ife sitiri ngati ana amene amangopita ndi chirichonse, koma ife timagwira chimene Mulungu akuchita ndi chimene analankhula ndi chimene adzachita, ndipo timamuona Iye akuchita icho ndipo ife timakhala ndi chimenecho. Kotero, Utumiki Usanu uli kuti, waperekedwera chiyani, kodi udzachita chiyani, kodi umagwira ntchito motani? Mafunso onse awa amene tikufuna kuyankha mu uthenga uwu lero ndi zina mwa zinthu zimene ife tikuyang'anapo mu nthawi ino pamene tikuyandikira mkwatulo.

Kotero, ife sitiri otengekatengeka uko ndi uku ndi kugwedezeka, ndipo apa pali chimene Iye ananena chimene Utumiki weni weni udzachita, "*Koma ndi kuchita zoona mwa chikondi tikakule mu zinthu zonse, kufikira Iye amene ali mutu ndiye Khristu kuchokera mwa Iye thupi lonse, lokowanidwa ndi kulumikizidwa pamodzi,*

pothandizanapo mfundo yonse, monga mwa kuchititsa kwa chiwalo chonse pa muyeso wache, lichita makulidwe a thupi, kufikira chimango chache mwa chikondi." Mwa kulankhula kwina ndi zophathikana palimodzi, kumangirirana wina ndi mzache, si matupi a wanthu awiri osiyana, si zikhulupiriro ziwiri zosiyana, sizingakhale kuti wina kukhulupirira ichi ndi wina kukhulupirira china. Paulo anati, "Zinthu izi zimene mwazimva kwa ine, mulankhule zomwezo ndikuphunzitsa ena kulankhula zomwezo," chifukwa Lingaliro la Khristu ndi Limodzi. Baibulo likuti munthu wa malingaliro awiri ndi osakhazikika mu machitidwe ache. Ife tonse tikuyenera kukhulupirira chinthu chimodzi, kuganiza chinthu chimodzi, kuyenda njira imodzi ndipo Mulungu wapanga njira. Iye anapanga njira kuti azichite izo kupyolera mu Utumiki Usanu monga mudzaona posachedwapa.

Kotero, kodi pali Utumiki Usanu, uli kuti Utumiki Usanu nanga umagwira ntchito motani? Pamene tipeza mayankho a izi, ife takhazikika pa chimene Mulungu akuchita. Kodi Utumuki Usanu uli kuti ngati ulipo? Inu mudzaona pamene tikupita ndipo ine ndikufuna inu muone pamene apa chimene iwo uli koyamba, ndipo kenako tifika ku chimene uli.

Ku Bukhu la Ahebri zikungotengera lemba limodzi ndipo ndikufuna ife tione chimene Mau akunena, zokhudza Utumiki Usanu ndi mtumwi kukhala m'modzi amene akhoza kugwira udindo uliwonse, ndipo mtumwi ndi amene amaimirira Khristu, ndipo mwa Mtumwi, Khristu akhoza kugwira ntchito iliyonse komanso mphatso zonse ngati kuli kofunika.

Tsopano pali amuna ena amene Khristu ali nawo monga, aneneri, alaliki, abusa ndi aphunzitsi. Ife tikumvetsa kuti si malo onse kumene kuli munthu ngati mlaliki, kulibe munthu oti akhale mphunzitsi, ndipo nthawi zambiri kulibe abusa ku malo ena, komabe Mkwatibwi akutenga chinthu chomwecho. Chifukwa ife tiri ndi Utumiki wa Utumwi zikutanthauza kuti tiri ndi m'busa, tiri ndi mphunzitsi, tiri ndi mlaliki, tiri ndi m'neneri ndipo zonse izi ziri momwemo. Ife tikudziwa kuti palibe amene akhoza kukhala mphunzitsi, mbusa, mneneri kapena mlaliki pokhapokha onse a iwo akuphunzitsa chimene mtumwi akuphunzitsa. Zikuyenera kukhala lingaliro limodzi ndi cholinga chimodzi, apo ayi ndiye kuti mukuika kusagwirizana mu Thupi ndi mu Mau. Paulo anawatsutsa ena chifukwa chokhala ndi chitsutso mu Thupi ndipo chitsutso chimatanthauza magawano…, monga wina kuphunzitsa chinthu china ndi wina kuphunzitsa chinthu china chosiyana polankhula za phunziro lomwelo. Pamene Mulungu amafuna kumuchotsa Paulo, Iye anamulora Paulo kulemba Mau a chinenero kuti awaike "kusunga" chinachake chimene Iye adzagwiritse ntchito mu tsiku lotsiriza. Chifukwa mu mpingo woyamba, Khristu anayang'ana ndikuona anthu atakhala pakati pa mpingo, ndipo Paulo anati, "Ine ndikangopita pali anthu amene adzauka ndikudzitengera okha ophunzira." Mwakulankhula kwina iwo analibe Mzimu womwewo umene Paulo anali nawo, ngakhale lingaliro lomwelo, iwo samagwirira chinthu chomwecho, iwo anali ndi

cholinga chodzimangira ufumu wa iwo okha…., koma ife tikumanga Ufumu wa Khristu mu nthawi ino.

Kotero, Utumiki Usanu uli kuti mu tsiku lathu? **Iwo waikidwa mu thupi koyamba mu udindo** wa Utumwi ndipo umapita ku maudindo ena pamene akuzindikira izi ndikubwera kumaitanidwe amene Mulungu akuwaitanira. M'busa, iye adzalalikira uthenga wa mtumwi. Ngati iye ali m'busa weniweni, iye sadzayesera kulalikira chinachake cha iyeyekha kuti iye apite njira yake ya iye yekha, chifukwa ndi mtumwi amene amazitenga kuchokera kwa Khristu moyambirira, kenako zimaonekera ku mautumiki ena. Kotero mu nthawi iyi pakhoza kukhala mipingo (magulu osonkhana) amene akhoza kukhala opanda m'busa, koma iwo ali nawo uthenga wa utumwi. Ndi chifukwa chake matepi awa, internet, ma cd, mp3 ndi mabukhu, afika paliponse padzikolapansi. Ine sindikukhulupirira pali malo alionse amene sanafike. Zikutanthauza kuti aliyense akutenga chomwecho chimene inu mukutenga ngakhale kuti iwo siali kuno. Zikutanthauza kuti pamene iwo akhala pansi ndikumvetsera tepi ku nyumba kwawo, iwo akutenga chinthu chomwecho molunjika kuchokera ku mpando wachifumu wa Mulungu, kudzera mu udindo wa mtumwi, ngakhale iwo asakhale ndi mlaliki, ngakhale iwo asakhale ndi mphunzitsi, ngakhale asakhale ndi m'busa zonse zikudzera mu uthenga wa mtumwi, ndipo iye amazikhulupirira izo. Mulungu wamuitana iye kukhala ku udindo wa ubusa ndipo akubwera ku lingaliro limodzi ndi cholinga chimodzi ndi mtumwi uja kulankhula chinthu chofanana, palibe magawano, kenako tikhoza kunena… pali abusa. Mukumvetsa? Chinthu chomwechonso ndi mlaliki ndi maudindo ena onse. Kotero pamene inu mumva chimene mtumwi akunena inu mumatenga zonse. Koma pali alaliki ena amene amafuna kubweretsa zinthu zawo kuti adzipezere ophunzira a iwo okha.

Mu masiku a Paulo pamene iye amalalikira Mau, panali iwo amene anakhala nawo kwa nthawi yaitali amene anali okanika, okhala ndi mzimu osiyana; koma mpingo sumatha kusiyanitsa. Zimaoneka ngati iwo amalalikira chinthu chofanana, kulalikira chinthu chomwecho, koma Paulo mwa vumbulutso la Mau a Mulungu amadziwa kuti kunsi kwa mitima yawo anali ndi cholinga chodzitengera ophunzira kapena kupita njira yawo, chimene ndi chizindikiro chimene Paulo anati mwana wa kuchionongeko. Chomwecho lero, Mulungu ali nawo uthenga, ndipo iye akudziwa mayendedwe a oipayo, chifukwa uthenga uwu wapita pa dziko lonse lapansi. Ndi uthenga wa Utumwi ndipo mwa iwo muli zonse zofunika kukapanga, aneneri, alaliki, abusa ndi aphunzitsi monga tawafunira.

Kotero Utumiki usanu ndi chiyani? Ndi chimenecho. Ndi utumiki wa utumwi kupita ku ndi ena kutenga vumbulutso lomwelo. M'busa ndi Mlaliki adzazimva izo ndipo adzazikhulupirira izo ndipo adzapita ndi kulalikira chinthu chomwecho. Paulo anati, "Pasakhale malekano pakati panu." Iye anati kwa Timoteo ndi Tito, "Zinthu izi mwazimva kwa ine, pitani kaphunzitseni zinthu zomwezi ndipo Ambuye akhale nanu."

Tsopano tiyeni titenge mtumwi uyu ku Ahebri, "Mtumwi," kukamba za Khristu. Akuti ku Ahebri 3:1, "*Potero, abale oyera mtima, olandira nao maitanidwe akumwamba, lingalirani za Mtumwi* (ameneyo ndi mtumwi wa Ayuda, Amitundu ngakhalenso wina aliyense) *lingalirani za Mtumwi ndi Mkuluwamsembe wa chivomerezo chathu, Khristu Yesu"* osati Yesu Khristu, koma Khristu Yesu. Iye anali Yesu Khristu asanapachikidwe pa mtanda, koma pamene anauka kwa akufa ndi Thupi la ulemelero ndi kubweranso mu Mzimu (Mzimu Woyera) pa tsiku la Pentekosite, Iye ndi Khristu Yesu. Ndipo tikuona kuti panali mtumwi pa tsiku la Pentekosite amene anali Petro, ndipo Mulungu anamupatsa Petro pamodzi ndi Mpingo wa Chiyuda chimene akanafuna kuti atsirize ntchito uthenga usanapite kwa Amitundu. Koma tsopano chimene ife tikuyang'anapo ndi anthu a Amitundu ndipo Mulungu kudzutsa munthu ndi kumupanga iye kukhala Kuwala kwa Amitundu. Tsopano kupitiriza kuwerenga, "*Lingalirani za mtumwi ndi Mkuluwamsembe wa chivomerezo chathu, Khristu Yesu amene adakhala okhulupirika kwa Iye amene adamuikayo, monganso Mose m'nyumba yache yonse."*

Tsopano ku Chipangano Chakale m'neneri anali wamkulu mu dongosolo la Utumiki wa Mulungu. Tsopano ichi ndi chofunika kwambiri, m'neneri anali wamkulu mu dongosolo la Utumiki. Inde panali Wamsembe Wamkulu, koma ntchito yake inali ya mtundu wina. Taonani apa, chiukitsiro cha Yesu Khristu chitachitika sipakutchulidwanso Mneneri. Izi ndizofunika kwambiri, chifukwa Iye ali mu udindo waukulu wa Mulungu ku Mpingo. Baibulo likuti, "Lingalirani za Mtumwi." Iye ndi Mtumwi ku dziko lonse, kwa aliyense, Ayuda ndi Amitundu, Mpingo wa Chiyuda, ndi Mpingo wa Amitundu. Iye anali pomwepo pa tsiku la Pentekosite. Ndipo pamene Mpingo wa Chiyuda unayamba kuyenda ndipo Mulungu anatenga namabala yake ya kwa Ayuda; kenako Iye anatembenukira kwa Amitundu. Iye adakali Mtumwi yemweyo, koma Iye anali ndi chinachake mu dziko kuti chiimirire Iye, kuonetsera Iye. Panali munthu apa kuonetsera Utumiki wa Khristu kwa Amitundu. Pamene Khristu anakwera kupita kumwamba, maudindo onsewa anali mwa Iye, Iye anali Mtumwi ndi Wamsembe Wamkulu. Kotero pamene anakwera kumwamba, Iye anapereka maudindo awa, kuwasiya pansi pano kuti akakhale mwa aliyense payekha payekha. Pakhoza kukhala mneneri, m'busa, pakhoza kukhala mphunzitsi ndipo pakhoza kukhala mlaliki ndipo onse awa kupitira palimodzi kukhala gawo la ichi. Koma sipangakhale mlaliki, sipangakhale mphunzitsi, sipangakhale m'busa kapena mneneri amene ali mu <u>dongosolo la ngwiro</u> osakhala gawo la Utumiki wa Utumwi. Inu mukhoza kusakhala nawo mautumiki amenewa mu madera anu. Mpingo uliwonse (gulu losonkhana) silingakhale ndi Mtumwi, kapena mlaliki, kapena m'busa kapena mphunzitsi. Koma ngati ali nawo Uthenga wa Utumwi uwu, iwo akulandira Mau omwewo. Mulungu yekha ndi amene akhoza kudzutsa munthu ndipo munthuyo adzanena kuti, "Ine ndikulalikira Uthenga wa Utumwi ndipo iye akhoza kulankhula kuti Mulungu wandiitana ine kukhala m'busa, chifukwa wandipatsa ine kukhala gawo la Utumiki wa Utumwi. Chabwino izi ndi mofanana ndi malemba. Inu simungakhale m'busa koma

osalalikira uthenga wa mtumwi. Paulo anati, "Zinthu izi wandimva ine pakati pa anthu ambiri, pita ukalalikire zomwezi." (Kugwiritsa ntchito chilankhulo chanu; koma kulalikira vumbulutso lomweli.)

Tsopano ine ndikufuna inu muone kufunika kwa izi; ife tonse timapeza uthenga wapamwamba wotere kuchokera ku gwero lake, Yesu Khristu Mtumwi komanso Wamsembe Wamkulu pamene akulankhula Mau ake choyamba kudzera mwa Udindo wa Utumwi. Tsopano pa mfundo iyi ine ndilankhula ichi, ku 1 Timoteo Chaputala 2, vesi 7 akuti: Paulo akulankhula kwa ndani, "*Umene anandiika ine mlaliki wache ndi mtumwi (ndinena zoona, wosanama ine), mphunzitsi wa Amitundu m'chikhulupiriro ndi choonadi.*" Tsopano taonani, Paulo anali mlaliki, mphunzitsi, mtumwi ndipo iyenso anakhudza udindo wa mneneri wa ku Chipangano Chatsopano ndipo anagwirapo udindo wa ulaliki kutenga Uthenga pamene iye amayenda mu dziko la mu nthawi yake.

Tsopano mu tsiku ili lotsiriza, Mulungu wapanga njira yofalitsira Mau kutali mosayenda mtunda wautali. Chimene ndikulalikira lero chifika kumaiko ambiri ngakhale lero pamene zikufika pa website ndikupita ku maiko osiyanasiyana. Pali anthu pa dziko lonse amene akulandira Uthenga wa Utumwi, ngakhale akhale opanda m'busa, mphunzitsi, mlaliki kapena mneneri mudera lawo. Koma tithokoze Mulungu, mu Madera ambiri Khristu ali ndi m'busa wa Umulungu amene akuti, "Ine ndikutsatira uthenga wa Utumwi." Mosafuna kubwereza bwereza, azitumiki onse adzalalikira vumbulutso lofanana, Mau ofanana, ndi Mzimu ofanana, ndi lingaliro lofanana, ndi cholinga chimodzi, onse palimodzi ngakhale akhale mlaliki kapena chiri chonse chimene chiri. Koma ngati inu mulibe mudera lanu, ndiye ife tiri nazo izo mu uthenga wa Utumwi. Paulo anati, ine ndine mtumwi, mphunzitsi, mlaliki ndipo mwantheradi Paulo anali m'busa kwa iwo amene amakhala mudera limene kunalibe m'busa oitanidwa ndi Mulungu.

Pamene tikuona za izi ine ndikufuna tipite ku Aroma, Chaputala 11, ine ndikumverera kuti ndizofunika kwambiri apa, ndipo pamene titsiriza, funso lidzayankhidwa, Utumiki Usanu uli kuti? **Uli mwa Khristu, kenako mwa Mtumwi, kenako umapita kwa anthu ena amene Khristu wawaika mu Utumiki uwu.** Pamene tikumva Paulo akunena, "Zinthu zimene ndi zosowa mu chisautso cha Khristu zimene zapanga ine." Mtumwi anapitiriza kunena, "Khristu anandiulurira ine vumbulutso limene linali lobisidwa dziko lapansi lisanalengedwe." Inu simunamumvepo Timoteo akulankhula ngati choncho. Munthu m'modzi yekha ndi amene amalankhula choncho, anali mtumwi amene Mulungu anamuika kunyamula ichi kwa Amitundu, chifukwa anali ndi cholinga chimodzi ndicho kutenga Mkwatibwi. Khristu akukonzeketsera Mkwatibwi Wake **ndicho chifukwa chake ife sitikuyesera kulalikira kwa Oyeramtima a kuchisautso. Khristu sakuchita ndi oyeramtima a kuchisautso mu njira yowaveka iwo Bafuta Wonyezimira, kuwakonzekeretsa mkwatulo; chifukwa iwo sakupita.** Iye ali naye Mkazi, ndipo akuchita ndi iye. Iye sakuchita ndi Israeli mu njira imeneyo, chifukwa akukonzekeretsa mkazi wake. Kukonzekera

ndi kumva komanso kulandira. Pamenepo muli okonzeka. Inu muli ndi lingaliro lomwelo limene Khristu ali nalo. Mamuna ndi Mkazi enieni adzakhala ndi lingaliro limodzi, kulingalira chinthu chomwecho, Baibulo likuti iwo ali amodzi. Paulo anati, "Ichi ndi chinsinsi chachikulu, koma ndikulankhula za Khristu ndi mpingo (Mkwatibwi)." Iye anati, "Iye amene alumikizidwa ndi Ambuye ali Mzimu umodzi," ndipo ali ndi Lingaliro limodzi, ali ndi cholinga chimodzi, ali ndi kukhumba kumodzi, mulibe magawano mwa Mkwatibwi weniweni ndi Khristu. Mkwatibwi pa dziko alibe magawano kapena chitsutsano ndi Khristu, iwo ali mwantheradi amodzi. Kotero Mulungu anaika udindo wa utumwi pano mu nthawi yotsiriza kuti adzatsirize za ukwati ndi kuika mu udindo umenewo mavumbulutso osungidwa onsewa pamene iwo akupita kuzungulira dziko lapansi. Kotero pobwereza.., ku dera kumene kulibe m'busa, kudera kumene kulibe mphunzitsi, kudera kumene kulibe mneneri, ngati iwo ali ndi Utumiki wa Utumwi, ali nazo zonse mwa kupereka kwa Mulungu.

Kodi pali Utumiki Usanu, nanga uli kuti? Funso limeneli layankhidwa tsopano. Anthu ambiri amene Mulungu sakuchita nawo adzakandabe mitu yawo, kudabwa ngati kulidi Utumiki Usanu, ndipo ngati ulipo uli kuti? Koma kwa Mkazi wa Khristu iwo ukuonekera kupyolera mwa udindo wa utumwi, lingaliro la Khristu limabwera choyamba kudzera mu udindo umenewo ndipo kenako kufalikira ku ma (udindo) mautumiki ena. Ndipo pamene ife tiyamba kulalikira ichi, Mkazi adzazigwira ndipo sangagwedezekenso gwedezekenso uku ndi uko ndi kutengeka ndi mphepo iliyonse ya chipembedzo, pamene tikulankhula chooanadi mu chikondi.

Ku Aroma, Chaputala 11:13, akuti apa, Paulo akulankhula…, *"Koma ndilankhula ndi inu anthu amitundu, popeza ine ndiri mtumwi wa anthu amitundu, ndilemekeza utumiki wanga."* Ine ndikufuna inu mudziwe kuti Khristu Yesu anali Mtumwi, osati kwa amitundu wokha komanso ngakhale ayuda. Koma Mulungu anadzoza munthu m'modzi kukhala mtumwi kwa Amitundu ndipo ameneyo ndi mtumwi Paulo. Ndipo pamene Mulungu anamuchotsa iye pa dziko namwali wa Khristu anagwa ku chikondi chake choyamba koma Mulungu anati, "Ine ndidzabwezeretsa Uthenga mu tsiku ili lotsiriza kuchokera pamene Paulo anasiira."

Ine ndiri ndi lemba lina apa, ndipo liri ku Aroma Chaputala cha 15, vesi 8. Likutiuza kuti Yesu Khristu anali Mtumiki wa kwa Ayuda ndipo anauza ophunzira Ake, kuti apite ku nkhosa zosochera za nyumba ya Israeli, asapite kwa Amitundu. Chifukwa chiyani? Chifukwa amadziwa kuti mu malingaliro a Mulungu pakanadzakhala winawake kuima m'malo mwake kubweretsa Kuwala kwa Amitundu. Paulo anati ku 2 Akorinto, 'Ife tiri m'malo mwa Khristu." Ife tilankhula chinthu chomwecho chimene Khristu akanalankhula ngati Iye akanakhala ataima apo. Ine ndikuvomereza chimene Paulo walankhula chimodzimodzi ngati kuti Yesu walankhula icho, chifukwa ndi chimene Paulo anali Iye kulankhula. Anali Khristu mwa iye chiyembekezo cha ulemelero!

Paulo anati, "Iwo amalemekeza Mulungu mwa ine," ndipo tsopano ndi Khristu mwa inu.

Tsopano Aroma Chaputala 15:1…, "*Kuti ndikhale mtumiki wa Yesu Khristu kwa anthu Amitundu."* Tsopano ine ndikufuna inu muone kwa ndani; kwa Amitundu osati kwa wina aliyense, kwa Amitundu, chifukwa Khristu akutenga kwa Amitundu anthu chifukwa cha dzina lache kukhala Mkwatibwi, kotero Paulo anati, "Ine ndine Mtumiki wa Yesu Khristu kwa Amitundu…," mwa kulankhula kwina Yesu Khristu sadzatsika kwa Amitundu mu thupi kuwalalikira iwo; koma anali naye munthu apa, ndipo iye anachita chimodzimodzi. Uthenga wa Paulo unali chimodzimodzi Yesu mwiniyekha kubwera mu thupi ndikulankhula. Khristu amalankhula kupyolera mwa Paulo, amene anaonetsera maudindo onse awa; chifukwa anati, "Ine ndine mlaliki, mphunzitsi, mtumwi" Kotero anati, Ine ndine mtumwi kwa Amitundu. Ine ndine Mtumiki wa Yesu Khristu kwa Amitundu kulalikira Uthenga wa Mulungu kuti kupereka msembe kwa Amitundu…, kuti Amitundu akalandiridwe poyeretsedwa ndi Mzimu Woyera." Paulo anati, "*Chifukwa chache ndiri nacho chodzitamandira cha Khristu Yesu ndi zinthu za mwa Mulungu. Pakuti sindingathe kulimba mtima kulankhula zinthu zimene Khristu sanazichita mwa ine zakumveretsa anthu amitundu, ndi mau ndi ntchito."* Chifukwa chiyani? Chifukwa anali nazo mwa iye zinthu zomwezo zimene zinali mwa Khristu tikanena za maudindo otumikira. Iye anali ndi Uthenga wa Amitundu, osati wa Ayuda, kotero amayenera kulalikira monga analalikira. Ndipo ine ndikulankhula kwa inu…, **"Ine sindikulankhula mochuluka za Oyeramtima a kuchisautso, ine sindikulankhula za Israeli mochuluka, kungokuonetserani tsiku ndi nthawi imene ife tikukhalamo, chifukwa ine sindiri mtumwi wawo." Ndipo tsopano Khristu akukwatira Mkwatibwi ndipo sindikulankhula za chirichonse koma chimenecho. Ndipo mkati mwa chimenechi, maudindo ena onse akuonekera.**

Pali alaliki; koma iwo adzalalikira chimodzimodzi chimene mtumwi akulalikira. Pali abusa; koma iwo adzalalikira chimodzimodzi chimene mtumwi akuphunzitsa. Ndipo pamene iwo achoka ku kulalikira zimenezo, iwo amadzichotsera okha ku madalatso a Mulungu. Paulo anati, "Lapani kuti mudzipulumutse nokha ku msampha wa satana." Ndi kotheka kuti mukhoza kudzipulumutsa nokha ku msampha wa satana. Ngati inu muli mtumiki weniweni wa Mulungu ndipo mwachoka, ndiye njira yokhayo yodzipulumutsira nokha ku msampha wa satana ndi…, sitepe yoyamba ndi kubwerera ku Mau – Uthenga wa Utumwi wa mu nthawi ino. Ngati inu muli woikidwa kukhala mu Utumiki Usanu umene ulipo pano, bwererani ku iwo, dzilumikizeni nokha ku iwo ndi kuchotsa malingaliro anu. Kukanika kwanu sikungakufikitseni kumeneko, zimatengera Mau. Kotero Paulo anati, "*Pakuti sindingathe kulimba mtima kulankhula zinthu zimene…"* zimene siziri zogwirizana ndi ntchito imene iye anapatsidwa. Iye anali ndi uthenga wopita kwa Amitundu kuti aukhulupirire, kuwapanga iwo kukhala omvera. (Aroma, Chaputala 15) Taoanani zimenezo, "*Mu mphamvu ya zizindikiro ndi zozizwitsa, mu mphamvu ya*

Mzimu Woyera; kotero kuti ine kuyambira ku Yerusalemu ndi kuzungulirako kufikira ku Iluriko, ndinakwanitsa uthenga wabwino wa Khristu. Ndipo chotero ndinachiyesa chinthu cha ulemu kulalikira uthenga wabwino, pamalopo Khristu asanatchulidwe kale, kuti ndisamange nyumba pa maziko a munthu wina. Mwakulankhula kwina, Uthenga wa Paulo unali woima pawokha. Khristu anali kudziimirira yekha, ndiye zimapita ku maudindo ena a mu Utumiki Usanu. Inde Paulo amaimirira Khristu, iye anali mtumwi amene Mulungu anamuika kwa Amitundu kuti akhale Kuwala. Ndi chifukwa chake iye amatha kuima mwamphamvu ndi kumuuza Timoteo ndi Tito, "zinthu izi zimene mwandimva ine ndikulalikira, pitani mukalalikire zinthu zomwezo mu lingaliro lomwelo, kukhala mu cholinga chimodzi, chifukwa kulalikira chirichonse chosiyana ndi ichi, Mulungu sadzadalitsa izo, koma polalikira ichi mukhoza kukhala wotenga mbali ndi chisomo chimene Mulungu wandipatsa ine."

Paulo anati mu vesi 21.., ***"Koma monga kwalembedwa, iwo amene uthenga wache sunawafikire, adzaona, ndipo iwo amene sanamve adzadziwitsa.*** *Chifukwa chakenso ndinaletsedwa kawiri kawiri kudza kwa inu;"* Tsopano akulankhula chiyani apa, padzakhala kudabwa kumene Mulungu ali nako pa iwo. Ena amati, "Ine ndimatsatira Brother Branham," ndipo ena amati, "Ine ndimatsatira Brother Jackson." Anthu awa alankhula zinthu zabwino ndipo atifikitsa pamene tafika; koma tsopano, Paulo anati padzakhala anthu amene adzakhala kwathunthu odzipereka, amene otsatira a Brother Branham ndi Brother Jackson sangathe kupereka nthawi yawo ya tsiku, iwo adzalankhula zinthu zosiyana siyana motsutsana nafe ndi kutitaya ngati oipa.., "MWA ICHI iwo sadzatsegula zitseko zawo ku uthenga UWU wapamwamba. Koma monga zalembedwera ku Aroma 15:21 Paulo anati iye, "Koma pali anthu awa (kwa Amitundu a lero) kwa iwo amene iye samamvekako, iwo adzaona ndipo iwo amene sanamve adzamva." Pali anthu amene akuona, pali anthu amene akumvetsa, ndipo pali anthu amene akukwera pa mapiko a mphungu ndi vumbulutso la Mau apamwamba awa.

Tsopano tiyeni tipite ku Chaputala cha 13 cha Bukhu la Machitidwe, ndipo ndikulankhula za…., "Kodi Pali Utumiki Usanu, Ngati Ulipo Uli Kuti? Uli pamene Mulungu anauika. Iye anauika mwa Khristu choyamba; kenako anauika mwa Paulo ndipo tsopano mu nthawi ino yotsiriza wauika mu Utumiki wa mu tsiku lotsiriza ndipo apo uli, musaziphonye izo, monga mautumiki (maudindo) onse a munthawi yotsiriza ali gawo la izo. Inde m'bale Raymond Jackson anali mtumwi, ndipo iye anaulura zinthu zambiri monga Mb'ado wa Mbiri isanayambe, Chiyambi ndi kugwa kwa satana, komanso angelo amene anagwa naye pamodzi. Mwa zina zimene iye anaulura chinali gawo lachiwiri la chisindikizo cha chisanu ndi chiwiri, chimene chidzachitika kwa Ayuda mu nthawi ya chisautso komanso mileniamu ndi zina zambiri. Koma pali uthenga umene ukugwirizana ndi Paulo ndipo ndi wa Mkwatibwi, Mkazi kukwatiwa ndi Iye, mai amene wakwatiwa ndi Iye. Ndipo mu Utumiki onsewu wa Utumwi muli mavumbulutso onse awa ndi mphatso izi zonse. Monga chala chachikulu

chikhoza kukhudza zala zina zonse, kutanthauza amuna amene akhoza kumva izi, ngakhale iwo amene sanaone, adzaona, ndipo iwo amene sanamvetse, adzamvetsa. Pamene zikupita ndi kupita pa dziko lonse, pali mphungu zazing'ono zimene zikumva…, ameneyo ndi Mkwatibwi kukonzekera pamene Iye akuvala Bafuta Wonyezimira, woyera ndi wopanda banga.

Ku Machitidwe, Chaputala 13:8, Paulo anapita kwa Ayuda ndi kuyesera kulalikira kwa iwo. Kenako pa vesi 44 la Chaputala chomwecho; akuti, "*Ndipo Sabata linalo udasonkhana pamodzi ngati mudzi wonse kumva Mau a Mulungu. Koma Ayuda pakuona makamu a anthu adadukidwa, natsutsana nazo zolankhulidwa ndi Paulo, nachita mwano.*" Ndi chinthu chomwecho mu tsiku lathu. Lemba ili linabwerezedwanso pamene ndinayendera mzinda wa Manila, Philippines mu 1997 kukachita kampeni ya choonadi ichi. Magulu ochuluka awanthu anatuluka mu mzinda ndipo anandifotokozera azitumiki amene anabwera kuti palibe nthawi iliyonse pamene zinachitika kuti anthu ochuluka choncho anabwerapo amene anali olumikazana ndi mautumiki a M'bale Branham ndi M'bale Jackson. (Zina mwa zithunzi ndi zoonera mukhoza kuziona pa wbsite yathu ku photo gallery- Philippines 1997) Nthawi yomweyo titangochoka ku Philippines panali mzimu wa njiru ndi umbuli pakati pa azitumiki amene anamva ndi kuona zinthu zazikulu zimene zimachitika mu misonkhano. Ngakhale ena mwa azitumiki omwewa anamuimbira Mtumwi Raymond Jackson ndi kutumiza malipoti abodza pa zomwe zimalalikidwa ndi kuchitika, ndipo iye analankhula motsutsa misonkhano imeneyi mogwirizana ndi malipoti. Ngakhalenso otsatira M'bale William Branham anayesera kuchepetsa zinthu zazikulu zimene Mulungu anachita mu misonkhano. **Zonsezi zinachitika chifukwa…, iwo sanathe kumvetsa kuti Mulungu amaulura vumbulutso lina mu Mau mu nthawi ino.** Zonse za zochitika izi ziri chimodzimodzi kwathunthu ndi Ayuda mu tsiku la Paulo.

Inde, m'mene zinaliri nthawi imeneyo, momwemonso ziri mu nthawi ino; iwo ayamba kutsutsa ndi kuchita mwano, kuyesera kubweretsa china chosiyana ndi Utumiki uwu wa Utumwi. Iwo amadzipatula okha kutenga ophunzira, koma chinthu chimodzi ndicho iwo sadzatenga m'modzi wa Mulungu ku icho, chifukwa mwa Mzimu Woyera iwo akudziwa kuti uyu ndi onyenga, sakulankhula chenicheni chimene Mau akulankhula, Utumiki wa Utumwi wa tsiku lathu ndi M'bado ndipo iwo akhoza kudziwa amene akulankhula. Inu mukhoza kunyenga ena mwa anthu nthawi zina, koma sumungathe kunyenga anthu onse nthawi zonse ndipo sungathe kunyenga Mkwatibwi. Iye adzadzuka. Iye sadzamva bwino nazo zimenezo, chifukwa Mulungu anaika Mzimu Woyera mwa iye ndi kumubatiza iye mu Thupi la Khristu. Mulungu anatipanga ife kukhala owonetsetsa pa Mau ndi kutipatsa ife lingaliro lodziwa Mau a Mulungu, ndipo tiri a lingaliro limodzi komanso cholinga chimodzi. Mu masiku a Paulo iwo anali mu lingaliro limodzi ndi cholinga chimodzi, mpingo woona, mpakana Mulungu anayamba kulora iwo kugwa. Iye anapalitsa ubwenzi Mkwatibwi kwa Khristu, ndipo tsopano mu nthawi ino pali Utumiki umene ukutikwatitsa ife

kwa Khristu. **Iwo a Uthenga wina amatsutsana ndi kuchitira mwano Uthenga wa Paulo.** Taonani chimene Paulo akulankhula kwa iwo pamene iwo amene amatsutsa ndi kuchitira mwano, vesi 46 akuti, *"Ndipo Paulo ndi Barnaba analimbika mtima ponena nati, Kunafunika kuti Mau a Mulungu ayambe alankhulidwe kwa inu."*

Tsopano ine ndikufuna inu muone ichi. Ine ndikufuna kuti ndichilankhule ichi pang'ono kuti zinali zofunika kuti Uthenga wa Utumwi uwu ulalikidwe kwa iwo amene adamva M'bale William Branham komanso M'bale Raymond Jackson, koma ambiri a iwo aukana iwo, okhawo osankhikawo akuyenda ndi Mulungu. Koma inu mukabwerera zaka zambuyomu, mauthenga 2000 mbuyomo, zaka zambiri pamene tinayamba mu 1950 zinali zabwino kuzibweretsanso kwa akuluakulu a mu dzina la Yesu ndi oyeramtima ena a ku chipembedzo amene anaitanidwa kuchoka mu zipembedzo ngati anamwali kuti ayambe ulendo wawo ngati Mkazi wa Khristu, monga Paulo anabweretsanso uthenga wake kwa Ayuda. Ine ndikukumbukira kulalikira za M'bale William Branham ndi kumalalikira za "Mneneri Wa Ku Chipangano Chakale Abwera Ku M'bado Wa Chipangano Chatsopano," ndipo iwo anati, ndi zofunika kukambirana. Koma mukuona zinali zabwino kuyamba kulalikira kwa iwo, zimayenera kupita kwa iwo motero choyamba pamene tinali mu mibado ya mpingo, ndipo chinangotembenukira mkati ndipo taonani pamene tiri lero. **Izi ndi za Mkazi wake wa Khristu yekha.** Mulungu watiulurira ife zinsinsi zimene zinabisika dziko lapansi lisanalengedwe…, **kuti mu udindo wa Utumwi muli ma udindo onse.** Mwakulankhula kwina, mtumwi akhoza kugwira udindo uliwonse wa utumiki weniweni. Kotero ngati inu mulibe abusa; inu muli naye m'modzi mu udindo wa utumwi. Ngati inu mulibe mphunzitsi, inu muli naye m'modzi mu udindo wa utumwi. Ngati inu mulibe mlaliki, muli naye m'modzi mu udindo wa utumwi. Ngati mulibe m'neneri, inu muli naye m'modzi mu udindo wa Utumwi. **Chala chachikulu chikhoza kukhudza zala zina zonse; ngakhale kuti sichingasandulike chimodzi cha zala zina.** Mulungu akudzutsa amuna amene akuyamba kugwira chinthu ichi. Koma pali ena amene amalowa ndipo amakonda m'mene zikumvekera, koma akangokhala kanthawi pang'ono ndi kuphunzira zinthu zina pang'ono, iwo amafuna kupita njira yawo. Kanthawi pang'ono amapezeka zawasokonekera, koma Mau a Mulungu amakhala akupitirirabe.

Taonani pamene tikuwerenga ichi tsopano; Paulo anati…, "Zinali bwino kulalikira izi koyamba kwa inu, kuti Mau a Mulungu alankhulidwe kwa inu koyamba, koma poona kuti inu mwawakana, ndi kudziweruza nokha wosayenera moyo osatha, taonani, ife tikutembenukira kwa Amitundu.' Ndipo ine ndikuti taonani, ife tikutembenukira kwathunthu kwa Mkwatibwi, taonani ife tikutembenukira kwathunthu kwa Mkazi wa Khristu. Pali anthu kunja uko kulalikira chiphunzitso cha mu mibado, ndipo Mulungu adzakhala nawo magulu ochuluka a iwo, Anamwali Opusa, Oyeramtima a Kuchisautso ndi zonse izo, koma ife tiri mu gawo losiyana, chifukwa mwa Mzimu umodzi tabatizidwa

mu Thupi limodzi. Ife tasandulika kuchoka mu ufumu wa Mibado ya Mpingo, kupita ku Ufumu wa Mulungu, mu Ufumu wa Kuwala (Akolose 1:13) ndipo tsopano apo tiri, osiyanitsidwa ndi dziko.

Tsopano taonani vesi lotsatira ku Machitidwe, Chaputala 13: 47.., "*Pakuti kotero anatilamulira Ambuye ndi kuti, Ndakuika iwe* (tsopano izi zikulankhulidwa kwa Paulo) *ukhale kuunika kwa Amitundu.*" Ndi chimene ife tiri. Mu nthawi ya Paulo, panaikidwa wina wake kukhala Kuwala kwa Amitundu, monga Khristu waika winawake mu nthawi ino kukhala Kuwala kwa Mkazi Wake wa Khristu. Alipo winawake amene akupereka malumbiro a ukwati lero tsopano, ndipo Khristu akutenga mkazi wake kulowa naye mu chihema ndipo dziko latsekeredwa kunja. Iwo amene anali wokonzeka analowa naye ndipo chitseko chinatsekedwa. "Ndakupanga iwe kukhala Mtumiki wa Mkazi uyu," chimodzimodzinso Paulo amapangidwa kukhala mtumiki kwa Amitundu, kuti apalitse ubwenzi Mkwatibwi. Kumbukirani Iye anatenga kuchokera kwa Amitundu anthu chifukwa cha dzina Lache kuti akhale Mkazi wache. "Ndakuika iwe ukhale Kuwala kwa Amitundu." Amitundu angaone bwanji pa dzikolapansi popanda Kuwala? Iwo amati ife tiri ndi Yesu, Iye ndi Kuwala. Inde, koma kodi Yesu anaimiriridwa ndi ndani mu tsiku limenelo? Anali Paulo. Iye anati, Paulo, "Ine sindibwereranso ndi kuzungulira kumalalikira kwa Amitundu, koma ndiika zonse izi mwa iwe ndipo iwe pita ukachitenso, ukakhale Kuwala kwa iwo. Ine ndakupanga iwe kukhala Kuwala kwa Amitundu kuti ukhale chipulumutso kufikira ku mapeto kwa dziko." Inu mukutanthauza kuti Mulungu anaika zochuluka motero mwa iye? Iye anali mtumwi ndipo anati yense amene akhulupirira, yense amene atsatira Mau, icho ndi chipulumutso chawo. Inu muli gawo la chisomo changa.

Tsopano tiyeni titenge vesi lotsatira, "*Ndipo pakumva ichi Amitundu,*" pamene Mkwatibwi anamva ichi, pamene Mkazi wa Khristu anamva ichi.., "*Ndipo pakumva ichi Amitundu anakondwera, nalemekeza Mau a Mulungu; ndipo anakhulupirira onse amene anaikidwiratu ku moyo osatha. Ndipo Mau a Ambuye anabukitsidwa pa dziko lonse.*" Abale ndi Alongo, mu tsiku lathu Mau a Mulungu akufalitsidwa pa dziko lonse lapansi, Mulungu wapereka njira. Palibe cholepheretsa. Taonani tsopano, iye anati; pamene Amitundu anamva ichi anakondwera ndi kulemekeza Mau. Pali anthu amene akukondwera ndi kusangalala pamene Ukwati ukuchitika, kotero tiyeni tisekere ndipo tinyadire! Ena adzati, padzakhala anthu angati tikalalikira zimenezo? Chabwino izo ziribe kanthu; Mkwatibwi adzalemekeza Mau a Ambuye. Iye adzalemekeza ndi kuyamika Ambuye! Mau akuti, "*Tikondwere, tisekerere, ndipo tipatse ulemerero kwa Iye; pakuti wadza ukwati wa Mwanawankhosa; ndipo Mkazi wache wadzikonzekera.*"

Tsopano ife tiri m'malo mwa Khristu ndipo pali malo amodzi amene akunena kuti, "Iye anasandulika tchimo kuti ife tikasandulike chilungamo cha Mulungu," ndipo ife timazivomereza izo, ife ndife chilungamo cha Mulungu ndipo ndife olungama monga Iye ali wolungama, chifukwa ife sitimanena za chilungamo chathu, koma timalankhula za chilungamo chake. Ku Akolose 1:13 akuti "*Amene*

anatilanditsa ife ku ulamuliro wa m'dima, natisunthitsa kutilowetsa mu ufumu wa Mwana wa chikondi chake amene tiri nawo maomboledwe mwa Iye mukukhululukidwa kwa zochimwa zathu." Ife tasandulika. Ife tatenga kale kusandulika kwathu kwa uzimu, ndipo tikungoyembekezera kwa thupi. Pali wam'thenga m'modzi yekha mu Baibulo amene analankhulapo za izo, pali wam'thenga m'modzi yekha amene analankhulapo mu Baibulo za mkwatulo, ndipo anali Paulo. Iye anati, "Akufa mwa Khristu adzayamba kuuka choyamba ndipo tidzasinthika mu kamphindi ndi kuthwanima kwa diso ndipo tonse tidzavala Bafuta Onyezimira woyera wopanda banga." Koma apa pali chimene ndikufuna kuti muone…, Paulo mtumwi kwa Amitundu anati ku Akolose, Chaputala 1:23, *"Ngatitu mukhalabe m'chikhulupiriro, ochirimika ndi okhazikika ndi osasunthika kulekana nacho chiyembekezo cha Uthenga Wabwino...,* ndipo iye akulankhula za "Uthenga Uwu," umene mwaumva , osati china chirichonse, (osati kwenikweni chimene Petro analalikira,) *umene mudaumva, wolalikidwa cholengedwa chonse cha pansi pa thambo; umene ine Paulo ndakhala Mtumiki wake"* Paulo anali amene amalalikira ndipo tsopano zapita ku zolengedwa zonse pansi pa Thambo. Ndi chinthu chomwecho ndi gawo iri lotsiriza. Taonani chimene akulankhula pa vesi 24; *"Tsopano ndikondwera nazo zowawazo chifukwa cha inu."* Paulo anasautsika mokondwa kuulura Khristu ngakhale zitengere chiyani, palibe chimene chinali chachikulu kapena chaching'ono, iye anaika moyo wache mu mzere tsiku lirilonse chifukwa cha icho. Ndipo osati zokhazo, koma kunapatsidwa kwa iye wanthenga wa satana kuti amugwetse, kumupanga iye kuti asadzikweze pamene iye anatengedwa kupita ku kumwamba kwachitatu ndipo Mulungu anamuonetsa zinthu zochuluka. Iye anati; "*Tsopano ndikondwera nazo zowawazo chifukwa cha inu,* kwenikweni kutenga malo a Khristu, tsopano tamuonani iye. Iye anati, "*Ndikondwera nazo zowawazo chifukwa cha inu, ndipo ndikwaniritsa zoperewera za chisautso cha Khristu m'thupi langa chifukwa cha thupi lache, ndilo Mpingo, amene ndinakhala mtumiki wache monga mwa udindo wa Mulungu umene anandipatsa ine wakuchitira inu wakukwaniritsa Mau a Mulungu:"* Chifukwa chiyani zinapatsidwa kwa iye? Sizinapatsidwe kwa iye mwa iyeyekha, koma zinapatsidwa kwa iye kukaonetsera Khristu kwa Mkwatibwi. Ndi chifukwa chake mauthenga awa akupita pa dziko lonse lapansi. Sizinapatsidwe kwa ndekha, koma kwa inu. Iye anati, ***"Wakukwaniritsa Mau a Mulungu."*** Ngakhale chinsinsi chimene chakhala chobisika mu mibado yambiri chaonekera tsopano. Kodi chaonekera motani? Chalalikidwa, ndipo chafalitsidwa.

Tsopano Utumiki Usanu, ife timagwiritsa ntchito Usanu, zikutanthauza atumwi, aneneri, alaliki, abusa ndi aphunzitsi. Mtumwi (chala chachikulu) chikhoza kukhudza zala (maudindo) zina. Mtumwi ameneyo akhoza kulalika ngati mphunzitsi, chifukwa iye ali mlaliki, iye ndi mphunzitsi ndipo ndi mtumwi. Paulo anati, "Ine ndine mlaliki, mphunzitsi, mtumwi." Chifukwa chiyani, chifukwa amagwira udindo umenewo. Iye anawauza azitumiki ena …, "Zinthu izi zimene mwazimva ndikulalikira, pitani mukalalikire vumbulutso lomweli ndipo pasakhale magawano pakati panu, mukhale mu Mau.

Sipangakhale kusiyana ngakhale pang'ono pa chiphunzitso. Iwo akhoza kugwiritsa ntchito chilankhulo chawo, koma **lingaliro** lidzakhala lomwelo, lingaliro limodzi, cholinga chimodzi ndi lingaliro la Khristu.

Tsopano pamene Mpingo unayamba kugwa mu tsiku la Paulo; iye anati, "*Koma ndiopa kuti maganizo anu angaipsidwe kusiyana nako kuona mtima ndi kuyera mtima ziri mwa Khristu.*" Izi ziri ku 2 Akorinto, Chaputala 11:2-3. Anthu ambiri amafuna kusokoneza chinthu ichi, anthu ambiri amafuna kugwiritsa ntchito mau akulu akulu, anthu ambiri amafuna kugwiritsa ntchito mau amene palibe aliyense amene akudziwa koma iwo, ndipo inu mumapita kutenga dikishonare kuti muone chimene iwo amatanthauza; koma Paulo anati, "Musachoke ku kudzichepetsa kuli mwa Khristu." Uthenga uwu ndi ophweka, musalore wina akusuntheni kukuchotsani ku iwo, inu mungokhulupirira Mulungu ndi kuyenda ndi Mulungu.

Kotero Utumiki Usanu uli kuti? Munthu wina posachedwapa anati kwa ine…, "Ngati mwakhala mukulalikira Utumiki Usanu kwa zaka makumi asanu ndipo tilibe iwo lero, ndiye kuti Mulungu akuzichita mu njira ina." Ameneyo anali satana kuyesera kulenga chikaiko. Khristu sazichita izo mu njira ina, Iye adzangochititsa khungu maso awo kuti asakhoze kuziona izo. Mkwatibwi aziona izo. Mkazi Wake aziona izo. Iwo aziona izo ndipo iwo adzakondwera nazo. Iwo adzaziona izo mu ulemerero wake onse ndipo ngati mutaona utumiki uwu lero, inu mukuona Utumiki Usanu mu Ulemerero wonse ndipo ena amakhala gawo la chisomo changa cha dongosolo lalikulu la Mulungu pamene Mwanawankhosa akutenga Mkazi wake kwa Iyeyekha mu mkwatulo. Ambuye adalitse Mkazi wa Mwana Wake wokondeka. Amen.

NDANDANDA WA MABUKHU A CHICHEWA

- Bukhu Lomasuliridwa La Chivumbulutso – Bukhu 1 (Chaputala 1-3)
- Bukhu Lomasuliridwa La Chivumbulutso – Bukhu 2 (Chaputala 4-8)
- Bukhu Lomasuliridwa La Chivumbulutso – Bukhu 3 (Chaputala 9-13)
- Bukhu Lomasuliridwa La Chivumbulutso – Bukhu 4 (Chaputala 14-18)
- Bukhu Lomasuliridwa La Chivumbulutso – Bukhu 5 (Chaputala 19-22)
- Chikhulupiriro Cha Mwana Wa Mulungu
- Chisomo Ndi Chifundo Cha Mulungu
- Kodi Pali Utumiki Usanu, Ngati Ulipo Ulikuti?
- Kulodzedwa Ndi Chipembedzo Cha Satana
- Mau Anachokera Kuti Kubwera Kwa Inu?
- M'mene Mulungu Amatilora Ife Kuti Tione Kulephera Kwathu
- M'neneri Wa Ku Chipangano Chakale Abwera Ku M'bado Wa Ku Chipangano Chatsopano
- Mau A Ulamuliro
- Umodzi Kupyolera Mu Utsogoleri

Mauthenga 1319 aliponso munakaseti kapena ma CD, DVD ndi VCD a mautumiki a kunja.

©2009 Sound of Liberty. Ufulu wonse ndi Wotetezedwa.